

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

MALANGIZO NDI CHILIMBIKITSO KUCHOKERA M'BAIBULO KUPITA
KWA AMENE AKULALIKIRA UTHENGA WABWINO

KUCHOKA PA BABELE MPAKA PA PENTEKOSTE KAPENA “MALILIME ENA”


“Ndipo Yehova anati,...Tiyeni, titsike, pomwepo tisokoneze chinenedwe chao, kuti wina asamvere chinenedwe cha mnzache... Chifukwa chache anatcha dzina lache Babele” (Genesis 11:6-9).

Chitapita chigumula chamadzi chachikulu m'nthawi ya Nowa, anthu anayambiranso kuchita zoipa pamaso pa Mulungu. Chifukwa cha kudzikiza mu mitima mwawo, iwo adayamba kumanga nsanja yofika mpaka kumwamba imene inatchedwa “Babele.” Pofuna kuthana ndi kudzikiza kwa anthuwo, Mulungu anawayankhulitsa zinenero zosiyanasiyana. Izi zisanachitike, “Dziko lapansi lidali ndi chinenedwe chimodzi ndi chilankhulidwe chimodzi” (Genesis 11:1). Popeza panalibe chinenero chofanana, umodzi wao unasokonezeka ndipo anthu anabalalika pa dziko lonse lapansi. Ichi chinali chinali chiyambi cha zinenero zosiyanasiyana za pa dziko lino.

Patapita zaka zopitirira 2000, pa tsiku la Pentekoste, otsatira a Yesu Khristu okwanira 120 anali ku Yerusalemu m'chipinda chapamwamba, kupempha kwa Atate mwa mtima umodzi. “Mwadzidzidzi anamveka mawu ochokera kumwamba ngati mkokomo wa mphepo yolimba...ndipo anadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera, nayamba kulankhula ndi malilime ena, monga Mzimu

anawayankhulitsa” (Machitidwe 2:2-4).

Chikhamu chachikulu, kuphatikizapo Ayuda kuchokera ku dziko lililonse la pansi pa thambo, chinasonkhana kuti chionetsetse chinthu chodabwitsachi. Popeza samazindikira chimene chimachitika, anthu



Pa Babele zilankhulo zinagawa anthu.

Pa Pentekoste, anthu anayanjanitsidwa

*Kudzera mu mphatso yodabwitsa ya zilankhulo
kuti Uthenga Wabwino umveke bwino lomwe.*

ena anawanena ophunzira aja kuti analedzera. Mulungu anali atatsanulira Mzimu Wake pa okhulupirira mwa Yesu Khristu ndipo anachitira umboni wa uthenga wabwino kudzera mu zizindikiro ndi zodabwitsa pamene ophunzira aja

amayankhula ndi “malilime ena.”

Zambiri zimanenedwa pakati pa a chipembedzo zokhudza “kuyankhula ndi malilime ena” ngati mmene zinachitikira pa tsiku la Pentekoste. Kodi chenicheni chimene chidachitika ndi chiyani? Kodi ophunzira aja amayankhula chiyani? Kodi “malilime enawa” ndi chinenero cha uzimu, kapena cha kumwamba, kapena cha angelo? Sitiyenera kusiyira akatswiri a zachipembedzo, kapena kudalira zimene ena zidawachitikira kuti tinene zoona za mphatso ya malilime. Mawu a Mulungu amaulula zenieni komanso zoona zake za mphatso imeneyi.

“Koma pochitika mau awa, unyinjira wa anthu unasonkhana, nusokonezedwa, popeza yense anawamva alikulankhula m'chilankhulidwe chache cha iye yekha” (Machitidwe 2:6). Nkhani iyi ndiyapafupi komanso yomveka bwino. Ophunzira aja samalankhula zosamveka m'chilankhulo cha angelo. Anthu awa a ku Galilea (ambiri anali asodzi osaphunzira) anali kulankhula mu malilime kapena ziyankhulo zoposa khumi ndi ziwiri za anthu amene adasonkhana. “Ndipo nanga ife timva bwanji, yense m'chilankhulidwe chathu chimene tinabadwa nacho?” (Machitidwe 2:8). Anthu ochokera ku Asia, Africa ndi ku

(Yapitirira pa tsamba 2)

Mau a Mkonzi
Tsamba 3

Kulankhula malilime

Chinenero cha
Pemphero

I Akorinto 14
Tsamba 10-11

Kodi mukudziwa?

Kuchokera ku chi Griki
Tsamba 4

Tsamba 5-7

Tsamba 8-9

Mafunso ndi Mayankho
Tsamba 11

Mau a pa Nyengo yake

Tsamba 12

Zimene

BAIBULO

Limaphunzitsa za...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;

Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;

Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;

Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;

1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;

1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;

Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba I)

Roma (Machitidwe 2:9-11) anali odabwa ndi ozizwa pamene anamva.

Ophunzira aja sadaziphunzire zinenerozi, koma mwa Mzimu Woyera, iwo anayankhula mu chinenero cha chilendo kutha anthu a ku maiko ena amve bwino lomwe. Ophunzira amalosera kapena kulalikira za Yesu Khristu mwana wa Mulungu wamoyo. “Akrete, ndi Aarabu, tiwamva iwo alikulankhula m'malilime athu zazikuru za Mulungu” (Machitidwe 2:11b). Mphatsoyi inali ndi olankhulawo osati anthu akumvawo. Mwachitsanzo, mwina Petro amalalikira kwa gulu lina mu chimodzi mwa zinenero za ku Asiya. Chapafupi pomwepo, mwina Yohane amalalikira kwa anthuwo m'chimodzi mwa zinenero za anthu a ku Arabiya.

Anthu pa Babele anagawanikana chifukwa cha chisokonezo popeza aliyense amalankhula chinenero chosiyana ndi cha mnezake. Pa tsiku la Pentekoste, anthu onse amatha kumva uthenga woyanjantisa wa Yesu Khristu kudzera mu mphatso yochokera kumwamba ya malilime. Ophunzira aja akadakhala kutha amangobolobosha, kunena zosamveka kapena kubuma chabe monga mmene anthu okhulupirira za “kulankhula malilime” amachitira lero, anthu akumvawo akadasokonezeka. Mmalo mwake, anthu a maiko onse anamva uthenga wa chipulumutso mu chilankhulo chawo.

Matamando akhale kwa Ambuye amene anawapangitsa ophunzira aja, kudzera mwa Mzimu Woyera, kuchitira umboni kwa alendo aliyense m'chinenero chake: kuchokera ku Babele mpaka pa Pentekoste; kuchoka ku chigawano kufika ku umodzi, kuchoka ku chisokonezo kufika ku chimvawo; kuchokera ku uchimo kufika ku chipulumutso.

-mws

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi uthenga wa mkalata umene umasindikizidwa m'dzina la Ambuye kwa anthu onse ku maiko onse ndi cholinga chofuna kuwakhazikitsa ndi kuwalimbikitsa mu choonadi cha Mau a Mulungu. Kalata uyu akuphunzitsa ndi kulimbikitsa zoona za Baibulo zimene zakhazikitsidwa kuyambira pa nthawi ya Khristu ndi ya atumwi.

Mau a Mulungu ndi okhawo amene ali muyeso wovomerezeka wa chikhulupiriro. Amaphunzitsa chipulumutso ndi mamasulidwe kuchokera ku uchimo kudzera mu ntchito ya maombedwe ya mwa Yesu Khristu; komanso kudzazidwa ndi Mzimu Woyera kumene kumatsatirapo. Ndipo kumatithandiza kutha tithandizira, tiwongolere ndi kuwapatsa ena mphamvu; komanso tikhale ndi chiyero choonekera pa gawo lililonse la moyo wa munthu kuphatikizapo mgwirizano ndi umodzi wa anthu a Mulungu. Utumiki wovomerezeka wa kwa Mulungu uli mu mwa anthu amene ubale wao wachikondi wazikika pa choonadi.

Akonzi: Michael & Rene Smith

KUTI MULANDIRE NAWO KALATAYI

Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi uthenga wa kalata umene timasindikiza miyezi itatu iliyonse molingana ndi chitsogozo cha Ambuye. Kuti mulandire nawo kalatayi mwaulere pa email, pitani pa intaneti ndipo mutipeza pa www.thegospeltruth.us. Muli omasuka kutitumizira maina ndi ma email a anthu amene akufuna kulandira nawo kalatayi. Mainawa muwatumize kwa mkonzi.

KUTI MUTIPEZE

Uthenga Wabwino wa Choonadi imasindikizidwa mu maiko osiyanasiyana kutha igawidwe m'maikowo. Ntchito yosindikiza kalatayi komanso mautumiki ena ochitika ndi ofesi yathu pothandiza kufalitsa uthenga wabwino amathandizidwa ndi zopereka zaufulu zoperekedwa mdzina la mpingo wa Mulungu.

The Gospel Truth, 605 Bishops Ct., Nixa, MO 65714 USA

editor@thegospeltruth.us

Mau a Mkonzi



"Pamenepo Petro, wodzala ndi Mzimu Woyera anati kwa iwo ..." —Machitidwe 4:8

Atadzazidwa ndi Mzimu Woyera, Petro sanagwe, kunjenjemera, kunena zosamveka kapena kutuluka thovu pakamwa; komatu analankhula molimba mtima, momveka bwino ndi mphamvu ya chikhulupiriro mwa Ambuye woukitsidwayo. Ndi dalitso lopambana kuzindikira choonadi cha kubatizidwa ndi Mzimu Woyera amene chimene chimatilimbikitsa ndiponso chimene chimatithandiza kuti tikhale ndi moyo wachiyero.

Mu kalata ino ya *Uthenga wa Choonadi*, ndikamba za mutu wa kulankhula malilime. Umenewu ndi mutu waukulu ndi wofunikira nchifukwa chake ndalemba zambiri. Ngakhale zili choncho, pali zambiri zimene tikhoza kulemba pa mutuwu. Baibulo limanena mwachimvekere zimene zinachitika pa tsiku la Pentekoste pamene ophunzira adayankhula malilime. Ophunzira anatha kulalikirira momveka bwino mu zilankhulo zomveka zimene iwo eni sanazidziwe chiyambireni chifukwa cha mphatso yopatulika ya Mzimu. Mdierekezi wapotoza zenizeni za chimene chidachitikachi ndipo wanyenga unyinji wa anthu poganiza kuti pali chilankhulo china chakumwamba ndipo kuti polankhula kapena kupemphera mwa voko ndi mawu osadziwika zimenezo zimachitika mwa Mzimu Woyera.

Kulankhula zosadziwika sikuchikita pakati pa mipingo ya chi Pente yokha ayi, komanso izi zimachitika pafupifupi mu chipembedzo chilichonse ndi cha chipembedzo cha Chikhristu chomwe. Ponena mosaopa kapena kupsatira, ndikufuna kunena pano m'dzina la Ambuye kuti mzimu wolankhula mobwebweta si Mzimu Woyera; izi zikusutsana ndi machitidwe, chiphunzitso komanso mzimu umene upezeka mwa Khristu ndi Mawu Ake. Ponena zimenezi, ena andinena kuti ndachimwira Mzimu Woyera. Indedi, andinena kale koma ndikuima pa kuwala kwa Mau a Mulungu ndiponso vumbulutso limene lye anandiululira la choonadi chimenechi.

Ndakumanapo ndi mzimu komanso mchitidwe wolankhula malilime a zosamveka osati kuno ku Amerika kokha komanso ngakhale ku maiko ena ambiri. Ndikamaphunzitisa abusa a mipingo yosiyanasiyana, palibe mutu wina umene umakwiyitsa Satana kuposa umenewu. Ndikufuna kutsindika kuti nkoyenera kutsata chitsanzo chimene Yesu anapereka popemphera ndi m'machitidwe ake.

Pa nkhani imeneyi yopemphera potsata mchitidwe wachikunja wobwebweta zosamveka, mipingo yambiri siitenga mbali koma imayima pakatikati. Munthu wina akavomereza mchitidwe woterewu, iye amatsekula khomo kuziphunzitso zochuluka zachikunja komanso ku mizimu imene sichokera kwa Mulungu. Kaya zimachokera m'maganizo, kaya malo, kapena ku mizimu yabodza, kubolobosha (kulankhula zosamveka) kumachokera kwa mdierekezi ndipo cholinga chake ndicho kunyenga anthu basi.

Ndizodabwitsa pakakhala akunja ndiponso pakhala anthu osakhulupirira Mulungu amene aonetsa mchitidwe wolankhula zosamvekawu umene ma Pente ndi ena amene amalankhula malilime amati ndicho chizindikiro chakuti anthuwo adzazidwa ndi Mzimu Woyera. Anthu ambiri otere amakhala m'moyo wauchimo koma amatchinjiriza uzimu wawo ndi mchitidwe wolankhula malilimewu.

Ndimakhulupirira kuti chimenechi ndi chimodzi mwa mphamvu zazikulu za zinyengo zimene mdaniyo wagwiritsa ntchito kuti alimbane ndi akhristu masiku ano. Tiyeni tipemphere ndikukhala tcheru nthawi zonse polimbana ndi mdaniyo. Mulungu atsekule maso amene ali mu mdima kuti aone.

Michael W. Smith

July 2014

Zambiri Zili pa

INTANETI

Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe


www.thegospeltruth.us

kuti mudzilandira

makalata athu kapenanso

kuti muone makalata

akale.



KUCHOKERA KU CHINENERO CHA CHIGRIKI

Dialektos (Dee-AHL-ek-toss)

Strong's Greek Dictionary: (njira ya) kulankhula mau, i.e. “chilankhulo”: chinenero, lilime.

Glossa (GLOSS-uh) Mawu a Chigiriki otanthauza “lilime” kapena “chilankhulo.”

Mau ochokera mchiGriki olembedwa ndi Thayer: Glossa:

1. Lilime, chiwalo cha thupi, chothandiza kulankhula.
2. Lilime, chilankhulo chimene anthu ena amalankhula anthu ena chosiyana ndi chilankhulo cha maiko ena.

Glossolalia (GLOSS-uh-LAY-lee-uh)

Mu kalata ino, mau akuti “glossolalia” atanthauza mchitidwe wa anthu kutulutsa maliwu koma osazindikira matanthauzo lake mu chinenero chimene palibe (mau/zoyankhula zopanda tanthauzo).

Mau oti Glossolalia achokera ku mau awiri a Chigiriki ndiwo: “*glossa*” (kutanthauza chilankhulo/chinenero kapena or lilime) ndi “*lalia*” (kutanthauza kunena kapena zolankhulidwa). Tanthauzo lake lenileni ndilo kulankhula chilankhulo chachilendo. Masiku ano, mauwa amawagwiritsa ntchito akatswiri a za chipembezidzo kutanthauza mchitidwe wa kulankhula kapena kupemphera chilankhulo chakumwamba kapena chilankhulo chauzimu (kubwebweta mau munga achitira anthu olankhula malilime masiku ano).

Dikishonale wolembe Merriam-Webster akuti:

“Kuyankhula kwambiri komanso kwaphuma koyeserera kuyankhula komveka komatu kawirikawiri zoyankhulazo zimakhala zosamveka komanso kopanda tanthauzo konse kwa omvera ndipo amayankhulira pa chipembezidzo.”

Xenoglossia (Zee-nuh-GLOSS-ee-uh)

Kuchokera ku mau awiri a chiGriki: *xenos* (kutanthauza wachilendo) ndi *glossa*. Akunena za pamene munthu akhoza kulankhula chinenero chachilendo chimene iye sanachiphunzirepo. Munthu amene akuchidziwa chilankhulochi angathe kuchimva. Ichi ndi chinenero chomveka.

Ndi kofunika kumvetsetsa tanthauzo la mau oti “malilime” munga mmene anawatanthauzira kuchoka ku chiGriki. Pali chiphunzitsa chabodza chimene chapangidwa chifukwa chosamvetsa bwino chinenero chimene Baibulo linalembedwera. Chifukwa chosamvetsa ndime yonse, pomasulira anatanthauzira molakwika. Mu mabuku a Machitidwe ndi 1 Akorinto, pena paliponse pamene pali mau akuti *glossa* akugwiritsidwa ntchito, akutanthauzira kulankhula malilime, ndipo izi zitanthauza chinenero chodziwika bwino. Sizitanthauza kulankhula zosadziwika kapena mmene masiku ano amagwiritsira ntchito mau akuti *glossolalia*.

Pa tsiku la Pentekoste, anthu a Mulungu analankhula zinenero za panso pano kwa anthu achilendo mu chinenero chawo cha alendowo. Ichi ndi chitsanzo cha zimene zimatchedwa kuti *xenoglossia*. Ndi

kofunika kudziwa tanthauzo la mau akuti “lilime” lichokera ku mau a mu Griki awiri otchedwa *dialektos* ndi *glossa* ndipo onse amagwiritsidwa ntchito koma mosinthanasinthana, zimene zikupereka chithunzi chakuti ophunzirawo amalankhula zinenero zimene zinali zodziwika bwino osati chinenero chimene amachidziwa iwowo.

Machitidwe 2:4 Ndipo anadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera, nayamba kulankhula ndi malilime ena [glossa].

Machitidwe 2:6 ...yense anawamva alikulankhula m'chilankhulidwe chache cha iye yekha [dialektos].

Machitidwe 2:8 Ndipo nanga ife timva bwanji, yense m'chilankhulidwe chathu [dialektos], chimene tinabadwa nacho?

Machitidwe 2:11 ...tiwamva iwo alikulankhula m'malilime athu [glossa] zazikuru za Mulungu.

Mphatso iyi ya malilime, munga zinachitikira pa Pentekoste, imamveka bwino munthu akamawerenga Malemba. Malemba akulongosola bwino za mphatsoyi, tanthauzo lake ndi mmene tingachitire nayo mphatso ya “malilime.” Komatu palibe pamene malemba atchula za kuyankhula zopanda tanthauzo kumene ena akuchita pa dziko lapansi. M'buku la Machitidwe, “kulankhula malilime” kukuchitika mwangwiro ndi mosalakwitsa munga momwe Mulungu adayipereker.

KULANKHULA MALILIME

BAIBULO NDILO KALOZERA WATHU

Mchitidwe wodabwitsa wa “kulankhula malilime,” kupemphera m’malilime ndi zina zotere, ulipo pakati pa akhristu ndi amene sali akhristu pa dziko lonse. Mchitidwewu ukufala kwambiri pa magulu a chikhristu mu dzina la Mzimu Woyera. Ndi kofunika kuti Mau a Mulungu akhale kalozera wathu ndi kuti zonse zimene timachita komanso ziphunzitso za mipingo yathu zigwirizane ndi zimene zalembedwa m’Baibulo – posalabadira za maganizo, zimene zimatchitikira kapenanso zimene zimaoneka pa matupi athu. “Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa chiphunzitso, chitsutsano, chikonzero, chilangizo cha m’chilungamo” (2 Timoteo 3:16).

CHENJERANI NDI ZIPHUNZITSO ZONYENGA

Yesu anachenjeza mpingo motere: “Chifukwa Akristu onama adzauka, ndi aneneri onama nadzaonetsa zizindikiro zazikuru ndi zozizwa: kotero kuti akanyenge, ngati nkotheke, osankhidwa omwe” (Mateyu 24:24). Mdierekezi samabwera ndi maonekedwe oipa okha komanso amabwera ngati mngelo wa kuunika wochita zodabwitsa. Ndi kofunikira kuchita choonadi ndi kukana chinyengo chilichonse. Ambiri akunyengeka ndi chiphunzitso chabodza chakuyankhula zosamveka ndiponso zopanda tanthauzo konse chimene chafala dziko lonse. Chiphunzitsochi chimapereka chitetezo chonama pa zauzimu kwa amene amachitsatira ndipo chimaderera zoonza zenizeni za Mzimu Woyera ndi kukhala mwachiyero. Kuyankhula malilime kwa masiku ano sizotsatira za Mzimu Woyera koma mzimu wonyenga. Nkofunika kuti mwana aliyense wa Mulungu azindikire zoonza za “malilime” ndipo akhale tcheru ndi bodza la ziphunzitso za masiku ano komanso zimene anthu amatsatira pa nkhani imeneyi yolankhula malilime.

KULANKHULA NDI MALILIME ATSOPANO

Yesu analamulira ophunzira ake kuti apite ku dziko lonse lapansi kukalalikira uthenga wabwino. “Ndipo zizindikilo izi zidzawatsata iwo akukhulupirira: m’dzina langa adzaturutsa ziwanda; adzalankhula ndi malankhulidwe atsopano; [glossa]” (Marko 16:17). Apa ndi malo okhawo mu mabuku a Uthenga Wabwino pamene akukamba za malilime ngati mphatso kapena chizindikiro. Zimenezi zinakwaniritsidwa mosangalatsa pa tsiku la Pentekoste pamene ophunzira “... anadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera, nayamba kulankhula ndi malilime ena” (Machitidwe 2:4) ndiponso “...yense

anawamva alikulankhula m’chilankhulidwe chache [dialektos] cha iye yekha” (Machitidwe 2:6). Ophunzira aja amalankhula mu zilankhulo “zatsopano” kapena zilankhulo “zina.” Iwo sadaziphunzire zilankhulozo koma anatero mwa mphamvu ndi mphatso za Mzimu Woyera.


Ophunzira aja samangobwebweta kapena kulankhula zosamveka. Iwo amalankhula momveka bwino komanso mosajejema m’chilankhulo chachilendo. Mwa Mzimu, iwo amayamba utumiki kwa anthu amene sanali Aisraele koma amitundu ina amene amalankhula zinenero zina.

Anthu ambiri lero amachitira umboni kuti anabatizika ndi Mzimu Woyera ndipo amalankhula malilime monga pa

tsiku lija la Pentekoste. Ngati zimenezi zili zoonza, anthu amenewa bwenzi akulankhula zinenero za anthu pofuna kuonetsera mphamvu ya Mulungu kusiyana ndi kungobolobosha zosamveka/zopanda tanthauzo ngati mmene zikukhalira m’mpingo yambiri lero.

MPHATSO YA MALILIME

Mtumwi Paulo analongosola momveka za kusiyana kwa mphatso zimene Mzimu amapereka. “Ndipo pali mphatso



ZIMENE ZINACHITIKA PA PENTEKOSTE

Ophunzira aja analankhula momveka bwino ndi mosiyana mu chinenero chachilendo.

(Yapitirira pa tsamba 6)



zosiyanana, koma Mzimu yemweyo” (1 Akorinto 12:4). Mzimu Woyera sapereka kwa anthu onse mphatso yofanana. “Pakuti kwa mmodzi kwapatsidwa mwa Mzimu mau a nzeru; koma kwa mnzache mau a chidziwitso, monga mwa Mzimu yemweyo: kwa wina chikhulupiriro, mwa Mzimu yemweyo; ndi kwa wina mphatso za machiritso, mwa Mzimu mmodziyo; ndi kwa wina machitidwe a mphamvu; ndi kwa wina chinenero; ndi kwa wina chizindikiro cha mizimu; kwa wina malilime a mitundu mitundu; ndi kwa wina mamasulidwe a malilime [glossa]. Koma zonse izi achita Mzimu mmodzi yemweyo, nagawira yense pa yekha monga afuna” (1 Akorinto 12:8-11).

Mulungu amapereka mphatso za Mzimu monga mmene akuonera kuti zipindulira thupi la Khristu komanso ntchito ya Ufumu wa Mulungu. Mphatso ya malilime, monga mmene zinaonekera pa tsiku la Pentekoste, ndiko kuthekera kolankhula chinenero chachilendo chimene sunachiphunzirepo koma imapatsidwa mwa mphamvu za Mzimu kuti tiwalalikire Uthenga wabwino kwa iwo amene ali eni ake a chilankhulo kapena chinenerocho. Mawu akuti “glossa” (kapena chilankhulo) amene akugwiritsidwa ntchito mu 1 Akorinto ndi omwewonso amene akugwiritsidwa ntchito mu Machitidwe 2. Imeneyi si mphatso yongobwebweta kapena kulankhula zosadziwika kwa munthu. Mphatso ya malilime siinali mphatso ya *glossolia* komatu ya *xenoglossia* ya Mulungu.

MPHATSO YA KUMASULIRA

Mphatso ya kutanthauzira malilime ndiyo mphatso yapadera ya Mzimu ya kumasulira zimene wina akulankhula mchinenero chake chimene ndi chosiyanana ndi chilankhulo cha anthu amene akumva zolankhulazo. Pa tsiku la Pentekoste, ophunzira aja akadakhala kuti sakudalitsika ndi mphatso ya malilime, akadafuna wina amene ali ndi mphatso ya kutanthauzira kuti amasulire uthengawo m’zilankhulo za anthu amene amalandira uthenga wawo. Nthawi zambiri, wina akamalankhula ngati zobwebweta, pamafunika munthu woti amasulire zimene zikulankhulazo. Izi zisiyanana kwenikweni ndi mphatso yoona ya malilime kapena mphatso yomasulira. Pamene pali mphatso ya malilime, sipafunikanso munthu womasulira zoyankhulazo popeza aliyense adzamva m’chilankhulo chake.

MPHATSO YA MALILIME SIINAPEREKEDWE KWA ONSE

Ambiri amafuna mphatso ya malilime ndipo amayilemekeza, ngakhale kuti samaidziwa kwambiri.

Paulo pa 1 Akorinto 12:31, anati “Koma funitsitsani mphatso zoposa. Ndipo ndikuonetsani njira yokoma yoposatu.” Kenaka, akunena za kuposa kwa ntchito za chifundo pa mutu 14. Akadakhala kuti anthu amasangalatsidwa komanso kuti akuika mtima pa chikondi monga mmene amachitira ndi malilime, dzikoli bwenzi lili lokoma zedi. Ngakhale kuti aliyense sangalandire mphatso yofanana kuchokera kwa Mzimu Woyera, onse akhoza kulandira Mzimu Woyera mwiniwakeyo ngati mphatso.

ZITSANZO ZA MPHATSO YA MALILIME

Kuonjezera pa tsiku la Pentekoste, pali malo awiri amene akupezeka m’malemba pamene anthu analandira Mzimu Woyera ndiponso analankhula malilime. Patatha zaka zingapo kuchokera pa tsiku la Pentekoste, Petro amalalikira kwa a m’nyumba ya Korneliyo ndipo Mzimu Woyera anawagwera onsewo. “Ndipo anadabwa okhulupirirawo akumdulidwe onse amene anadza ndi Petro, chifukwa pa amitundunso panathiridwa mphatso ya Mzimu Woyera. Pakuti anawamva iwo alikulankhula ndi malilime, ndi kumkuza Mulungu” (Machitidwe 10:45-46).

Zitachitika izi, Petro anachitira umboni kuti “...Mzimu Woyera anawagwera, monga anatero ndi ife poyamba paja” (Machitidwe 11:15). Chimodzimodzinso, Mzimu Woyera anafika pa ophunzira a Yohane M’batizi amene analandira Khristu ku Efeso. Iwonso “...analankhula ndi malilime [glossa], nanenera” (Machitidwe 19:6).

Mzimu Woyera sunaperekedwa kwa anthu pa tsiku la Pentekoste komanso unaperekedwa kwa okhulupirira onse amene atsegula mitima yawo ndi kukhumba kudzazidwa. Mulungu anaperekanso mphatso ya malilime mu zitsanzo zimenezi munga mmene anachitira pa Pentekoste. Pa nthawiyinso anthu samalankhula zosamveka, koma amalankhula mu zinenero za anthu amene anabwera kudzamva mau. Zonena zina zotsutsana ndi izi, ndizopotoza zimene Malemba amanena momveka. Kudzera mu mphatso ya zilankhulo zosiyanasiyana zachilendo, iwo ananenera, kapena anaphunzitsa ziphunzitsa za Khristu m'zilankhulo zimenezo.

SI ALIYENSE AMENE AMALANKHULA MALILIME

Mipingo yambiri imene imalankhula zilankhulo zosadziwika, imaphunzitsa kuti chimenechi ndi umboni wa Mzimu Woyera. Kumeneku nkusonyeza kuti chidziwitso chawo cha malilime n'cholakwika. Komanso n'kulakwa kukhulupirira kuti aliyense adzalankhula malilime olondola munga momwe zinachitikira m'Baibulo. Mulungu amayika ziwalo m'thupi ndipo amagawa mphatso za Mzimu munga momwe kumukomera lye. Paulo pa 1 Akorinto 12:28-30 anafunsa mafunso pofuna kutsindika nkhanayi anati "Kodi ali onse atumwi? Ali aneneri onse kodi? Ali aphunzitsi onse? Ali onse ochita zozizwa?" Yankho la mafunso onsewa ndilo "Ayi." Paulo akupitira kufunsa kuti, "Ali nazo mphatso za machiritso onse kodi? Kodi onse alankhula ndi malilime? Kodi onse amasulira mau?" Yankho lake la mafunso onsewa likhala lomwe lija: "Ayi."

MALILIME (CHINENERO CHACHILENDO) NDI IMODZI MWA MPHATSO

Pamene ophunzira 120 aja m'buku la Machitidwe 2 analankhula mu zinenero zachilendo, ena ambiri amene adalandira Mzimu Woyera pa nthawiyi sanalankhule nawo malilime (zinenero zina). Pamene anthu aku Samariya anamva Mau a Mulungu ndi kupulumutsidwa, Petro ndi Yohane anawapempherera ndipo analandira Mzimu Woyera (Machitidwe 8:14-17). Iwo sanalankhule malilime. Nayenso Paulo sanalankhule malilime nthawi imene adalandira Mzimu Woyera. Chopambana kwambiri nchakuti Yesu naye sanalankhule malilime pamene Mzimu Woyera anatsika pa lye.

Silidali lamulo lakuti anthu azilankhula malilime, kapena chinenero chachilendo. Anthu odzazidwa ndi Mzimu Woyera sanayankhule malilime. Ngakhale Yesu sanachite ichi. Kuyankhula malilime idali mphatso imodzi ya Mzimu imene idaperekedwa pa nthawi yake yoyenera kuti tichitire umboni kwa osakhulupirira kuti Uthenga Wabwino ufalikire ndi kuti iwo akhulupirire uthengawo (1 Akorinto 14:22).

Umboni wa Mzimu ndiwo Mphamvu Yokhalira moyo Wachiyero

Umboni weniweni wa Mzimu Woyera upezeka mu mphamvu zakukhala moyo wachiyero ndi kubereka chipatso cha Mzimu (Agalatiya 5:22-23). Ndi kudzera mu chipatso chimenechi pamene moyo wauzimu wa munthu umaonekera kwenikweni. Pali anthu ambiri amene amangobolobosha ndi kumalankhula zosamveka. Iwo amanena kuti ali ndi Mzimu Woyera, komatu Mzimu umakhala m'kachisi woyera ndi wopatulika.



Kulankhula malilime, kapena
zinenero zachilendo, sikunalamulidwe,
komanso sikunachitike ndi anthu onse amene
anadzazidwa ndi Mzimu Woyera
ndipo Yesu Mwini sanapereke chimenechi ngati chitsanzo


KUMALIZA

Malemba amakhazika ndondomeko yomveka bwino ya zimene zinachitika pa Pentekoste pofuna kumvetsetsa bwino lomwe za mphatso ya malilime munga chilankhulo chachilendo cha anthu. Mchitidwe wolankhula malilime wakopa unyinjira wa anthu padziko lonse amene amafunitsitsa atalankhula kuti aoneke auzimu kwambiri. Munthu akakhala ndi mchitidwe wotere, koma nakhala m'moyo wauchimo, nchifukwa chiyani iye alakalaka kulankhula mwa Mzimu Woyera munga zinaliri m'Baibulo? Kulankhula zosadziwika sikotsogozedwa ndi Mzimu Woyera koma kotsogozedwa ndi mzimu wachinyengo wotsutsana ndi Mulungu. Mulungu safuna kupembedzedwa mu njira zimene zili zosavomerezeka. Chidzalo cha Mzimu Woyera sichipezeka mu zionetsero za kunja koma mu chilungamo, mtendere ndi chimwemwe.

-mws

Chilankhulo cha Pemphero

“Chilankhulo cha Angelo”



Palinso chiphunzitso china chonyenga chimene chifanana ndi mchitidwe wolankhula zosadziwika. Umenewu ndi mchitidwe wopemphera m'malilime umene utchedwa “chilankhulo cha pemphero” kapena “chilankhulo cha angelo.” Anthu ena amachita mchitidwewu pagulu ndipo anthu enanso amaphunzitsa kuti ndi “chilankhulo cha pemphero chimene munthu amalankhula payekha.” Pamene anthu apemphera m'njira yotere, iwo amalankhula mau ndi kutulutsa maliwu amene satanthauza kanthu kwa iwo eni kapenanso owamverawo.

Komanso, choonadi sichidziwika ndi zimene wina wake wakumana nazo koma ndi Mau a Mulungu. Pamene mchitidwe uwu uyesedwa ndi malemba, uonetsa kuti ichi ndi chiphunzitso chimene munthu wangopanga, osati chochokera kwa Mulungu – popeza sizili m'malemba.

TIKULAMULIDWA MMENE TINGAPEMPHERERE

Amatiphunzitsa kupemphera “...ndi kupemphera mu Mzimu Woyera,” (Yuda 1:20) ndi kupemphera nthawi zonse “...mwa pemphero lonse ndi pembedzero mupemphere nthawi yonse mwa Mzimu” (Aefeso 6:18). Zimatengera Mzimu Woyera kutitsogolera ndi kutithandiza kuti tidziwe kupemphera molingana ndi chifuniro cha Mulungu. Tiyenera kupemphera moona ndi modzikhuthula kwa Mulungu, ndiponso kukhala mu chiyero ndi kupemphera panso pa chitsogozo cha Mzimu Woyera.

MZIMU AMATPEMPHERERA

Ena amatenga mau a pa Aroma 8:26b amene amanena kuti “...Ndipo momwemonso Mzimu athandiza kufoka kwathu; pakuti

chimene tizipempha monga chiyenera, sitidziwa; koma Mzimu mwini atipempherera ndi zobuula zosatheka kuneneka.” Malemba amenewa amapeputsa chiphunzitso cha chilankhulo cha pemphero cha anthu amene amatama pemphero la chilankhulo. Mzimu adzatipempherera “ife” osati “kudzera” mwa ife. Ndimayi ikupitiriza kunena kuti kubuula kwa Mzimu “kosatheka kuneneka” kapena kulankhulidwa. Choonadi cha ndimeyi ndicho chakuti Mzimu wa Mulungu amatithangatira komanso kutithandiza kutumikira ku nkhwana zimene zimakhudza moyo wathu mozama.




Angelo...sanalankhule
zosadziwika, komatu analankhula
mu chinenero cha munthu amene
akumverayo.

MALILIME A ANTHU NDI A ANGELO

Zimene Paulo analemba pa 1 Akorinto 13:1 ambiri amazigwiritsa ntchito pofuna kuvomereza za kulankhula kapena kupemphera mu chilankhulo cha angelo. “Ndingakhale ndilankhula malilime a anthu, ndi a angelo.” Mau akuti “ndingakhale”; adawamasulira kuchokera ku Chigriki otchedwa “ean” amene amatanthauza nthawi yamuyaya kapena yosatsimikizika. Mau a Chigrikiwo amasulidwa bwino ndi mau akuti: “ngakhale.” “Ndikadayankhula zilankhulo za anthu ndi za angelo...” Paulo samatha kuyankhula zilankhulo zonse za anthu ndi za angelo. Sanathe kusuntha mapiri ndiponso sanapereka thupi lake kuti aliotche. Paulo

amanena za zinthu zimene sizinachitike pofuna kutsimikiza mfundo ya kufunika kwa ntchito za chifundo kuposa zonse.

Tingathe kumvetsa bwino za “malilime a angelo” kumene ndikulankhula mopanda chibwibwi komanso kuyankhula bwino. Ngati anthu akadatha kupemphera kapena kuyankhula chilankhulo cha angelo, chingakhale chanzeru kuona mmene angelo amalankhulira padziko lapansi. Muli zitsanzo zambiri m’malemba zimene zingatithandize kudziwa izi. Angelo adalankhula ndi Zakariya (Luka 1:13), ndi Mariya (Luka 1:30), ndi abusa oweta nkhusa (Luka 2:10), ndi Petro (Machitidwe 12:8) ndi ena ambiri. Angelowa, amene ndi amithenga opatulika a Atate, sanalankhule zosamveka kapena zopanda tanthauzo, koma analankhula chilankhulo cha anthu amene amalankhula nawo.



Mau a pa 1 Akorinto 13:8

akupitirira kunena kuti: “Chikondi sichitha nthawi zonse, koma kapena zonenera zidzakhala chabe, kapena malilime adzaleka, kapena nzeru idzakhala chabe.” Akadakhala kuti malilime ndi achingelo, angatonthole bwanji? Kodi angelo angalephere kulankhula? Paulo sadanenepo kuti adalankhula chilankhulo cha angelo ndipo Malemba sanena kuti Paulo adalankhulapo chilankhulo cha angelo.

MAU AKUTI “ZOSADZIWIKA” ANAWAONJEZERA M’ZOLEMBA ZINA

Mapente ndi ena amaphunzitsa “za chilankhulo cha kupemphera munthu payekha” 1 Akorinto 14:14. “Pakuti ngati ndipemphera m’malilime, mzimu wanga upemphera koma chidziwitso changa chikhala chosabala kanthu.”

Mawu akuti “Glossa” awagwiritsa ntchitonso, kutanthauza chilankhulo chachilendo—osati kuyankhula zosamveka/ zopanda tanthauzo. Kungathe kutanthauzira malembo molakwitsa kusintha tanthauzo la mawu oti “glossa” mwadzidzidzi kuti atanthauze za kupemphera zosamveka.

Ngati munthu akupemphera mu chilankhulo chachilendo, izi sizipindulila munthu amene akumvera chifukwa sangamve chilankhulo ngati chilankhulocho sichobadwa nacho. Ngati munthu apemphera m’chilankhulo chachilendo, kodi “nanga iye wakukhala wosaphunzira adzati Amen bwanji, pa kuyamika kwako, popeza sadziwa chimene unena?” (1 Akorinto 14:16). Paulo adati “amene sadaphunzire chilankhulocho sangalimve pemphero, osati

popeza linali lachibwana, koma popeza sanaphunzitsidwe chilankhulo chachilendocho. Munthu amene adaphunzira chilankhulocho angathe kumva pempherolo. Koma pempheroli lingakhale lopanda phindu komanso silingadalitse aliyense amene sakutha kulankhula chilankhulocho.

LAMULO LA YESU SILILOLA KUBWEREZABWEREZA

Ngakhale anthu amaphunzitsa ziphunzitso zotani, tiyeni tione chitsanzo Yesu Mwini monga momwe adatiphunzitsira zomwe tiyenera kuchita pakupemphera



Ndipo popemphera,
musabwerezebwereze chabe iai,
monga amachitira anthu akunja.

Mateyu 6:7-13

m’buku la Mateyu 6:7-13. “Ndipo popemphera, musabwereze-bwereze chabe iai, monga amachita anthu akunja...” (7). Mau a chiGriki otanthauza “kubwereza-bwereza” atanthauza chibwibwi. Apatu m’zoonekeratu kuti tiyenera kupemphera momveka komanso osachulutsa gaga m’diwa. Akunja komanso achigololo amalankhula mobwerezabwereza m’mapemphero awo. Yesu adaletsa kutero. Izi ndizo zimene ambiri opemphera “malilime” amachita. Amaphunzitsa anthu kupemphera pakubwereza chinthu chimodzimodzi kambirimbiri, zimene zitsutsana ndi Mawu a Mulungu.

Mu ndime 9, Yesu akunena kuti, “Chifukwa chache pempherani inu chomwechi.” Yesu sadalankhule maliwu achilendo kapena kulankhula chilankhulo chachilendo. Adapemphera mwachindunji komanso zomveka. Mulungu akadafuna anthu Ake kupemphera mosiyana m’chilankhulo chosadziwika, Yesu akadatiphunzitsanso chomwecho; ndipo tikudziwa kuti Yesu ndiponso Atate sakutsutsana koma ndi amodzi.

OSANYENGEDWA NDI ZIPHUNZITSO ZA ANTHU ZABODZA

Palibe umboni kapena zitsanzo m’Baibulo zokhudza chilankhulo cha angelo. Izinsu ndiko kupotoza choonadi ndipo si za Mulungu. Musatengeke ndi zikhulupiro komanso ziphunzitso za anthu, koma tsatani chitsanzo cha Khristu kuti mupezeke okonzeka kukumana naye mu mtendere akamabweranso.

-mws

1 Akorinto 14

Komatu ndi masiku ano pamene Akhristu adayamba kusanthula malemba kuti akwaniritse zolankhula potengera mmene munthu akumvera m'maganizo mwake, komanso zosamveka. Kulankhula motere sikunayambe ndi Khristu koma kudalipo kale pakati pa anthu akunja. Mchitidwe uwu wachikunja m'matchalitchi masiku ano ndiwo waphuma komanso mzimu wonama. Zolankhula potengera zakuimvaimva za m'thupi anthu amaziona molakwa ngati za umulungu komanso zauzimu. Kuyankhula komanso kupemphera zosamveka sikumachitika m'matchalitchi masiku oyambirira komanso sikuchitika m'tchalitchi la Mulungu masiku ano.

Chisokonezo chachikulu komanso chiphunzitso chonama zichokera pa kusachita molondola zimene mau amene ali pa 1

Akorinto 14 akunena pamene Paulo adalankhula za mchitidwe wa kulankhula malilime.

Chisokonezo chachikulu chichokera kwa munthu osati ku Mau a Mulungu. Pa tsiku la

Pentekoste, Mulungu adakhazikitsa mmene mphatso ya malilime iyenera kukhalira. Mau akuti “*glossa*” (chilankhulo chachilendo), amene adagwiritsidwa ntchito m'buku la Machitidwe 2, akugwiritsidwanso ntchito m'buku la 1 Akorinto 14. Tikaona zimene zidachitika pa tsiku la Pentekoste, tiyenera kumvetsa mosavuta chiphunzitso cha Paulo ku mpingo wa kwa Akorinto.

Mzinda wa Akorinto udali dooko lalikulu la anthu ochokera kosiyanasiyana komanso achikhalidwe chosiyanasiyananso. Mudali mavuto ambiri pakati pa anthu a mu mpingo ndipo Paulo adawauza mwachindunji m'buku la 1 Akorinto 3:3, “Pakuti pokhala pali nkhwidzi ndi ndewu pakati pa inu simuli athupi kodi....” Buku la 1 Akorinto ndilo buku lodzudzula ndi kukonzanso anthu a mumpingowo amene anali ankhwidzi komanso samatsata khalidwe la Chikhristu.

Tikasanthula mosamala mutu 14 tiona kuti Paulo samaphunzitza

mchitidwe wachilendo wa malilime koma amawadzudzula chifukwa mchitidwe wolemekeza molakwika komanso kugwiritsa ntchito molakwika chilankhulo cha chilendo. Padali chisokonezo pakati pa mpingo. Ngakhale kuti zinali zotheka kuti wina adali ndi mphatso yooni ya malilime mu mpingo ndipo amalankhula chilankhulo chachilendo chimene sadachiphunzire, koma mwina zikhoza kukhala kuti sizinali choncho, popeza Mulungu si gwero la chisokonezo. Nkutheka kuti anthu amene amadziwa kale zilankhulo zachilendo amazilankhula popanda chivomerezo cha omvera amene samadziwa chilankhulo cha chilendocho. Anthu awa sanali ndi mphatso yooni ya malilime popeza siidapatsidwe mwauzimu. Paulo akuwalamulira kuti apemphe Mulungu mphatso ya uneneri (kualikira) imene mpingo ikathandiza kuti

mpingo umangiririke. Uthenga wa kwa Mulungu m'chilankhulo cha munthu amene akumvera ukadapindula kwambiri kusiyana ndi chionetsero chonyada chakulankhula m'chilankhulo cha chilendo.

Ganizirani mavesi angapo kuchokera m'buku la 1 Akorinto 14 ndi zimene atanthauza—poganizira kwenikweni tanthauzo la malilime kuti ndi chilankhulo cha chilendo. (Dziwani ichi: M'Baibulo

la Chingerezi la KJV mau akuti “osadziwika” adawaikamo ndi anthu amene amatanthauzira. Mauwa mudalibe m'mabuku oyambirira ndipo adasiidwa m'mabaibulo otsatira.)

Pakuti iye wakulankhula lilime salankhula ndi anthu, koma ndi

Mulungu; pakuti palibe munthu akumva; koma mu mzimu alankhula zinsinsi. (vesi 2)

Munthu amene ayankhula za zozizwa za Mulungu m'chilankhulo chachilendo sayankhula ndi anthu koma ndi Mulungu ngati anthu amene alipo akumva zolankhula zachilendocho. Mu ndime **2 mpaka 3**, Paulo akutsindika za kufunika kwa kunenera pakukweza mpingo. Munthu amene akuyankhula chilankhulo chachilendo akudzimangirira yekha popeza ndiye yekha amene akumva zimene iye akulankhula.

(5) Ndipo ndifuna inu nonse mulankhule malilime, koma makamaka kuti mukanenere; ndipo wakunenera aposa wakulankhula malilime, akapanda kumasulira, kuti Mpingo ukalandire chomangirira. (6) Koma tsopano, abale, ngati ndidza kwa inu ndi kulankhula malilime, ndikakupindulitsani chiyani, ngati sindilankhula ndi inu kapena m'vumbulutso, kapena m'chidziwitso, kapena m'chinenero, kapena



“Paulo samaphunzitza machitidwe achilendo a kulankhula malilime koma amawadzudzula chifukwa amagwiritsa ntchito molakwika zilankhulo zachilendo.”

m'chiphunzitso? (onaninso mavesi 12-13)

Paulo akadasangalala ngati anthu onse akadamalankhula chinenero zosiyanasiyana koma adawauza kuti apeze mphatso zimene zingakweze mpingo (osati zilankhulo za chilendo zimene ziyambitsa chisokonezo). Kunenera ndikopambana ngati pali wina amene angamasulire chilankhulo chachilendocho kuti mpingo wonse uthandzidwe. Chipindulanji kwa Paulo kuyankhula zilankhulo zosiyanasiyana ngati palibe wina amene angamve zilankhulozi?

(9) Momwemonso inu ngati mwa lilime simupereka mau omveka bwino, kudzazindikirika bwanji chimene chilankhulidwa? Pakuti mudzakhala olankhula kumlengalenga.

(10) Ilipo, kaya, mitundu yambiri yotere ya mau pa dziko lapansi, ndipo palibe kanthu kasowa mau. (11) Chifukwa chache, ngati sindidziwa mphamvu ya mauwo ndidzakhala kwa iye wolankhulayo wakunja, ndipo wolankhulayo adzakhala wakunja kwa ine.

Ngakhale mawu akhale oona bwanji adzangopita pachabe ngati alankhulidwa m'chilankhulo chimene omvera sachidziwa. Pali zilankhulo zambiri zachilendo m'dziko lapansi ndipo zilankhulozi zili ndi matanthauzo. Koma, ngati simukumva zilankhulozi, zimamveka chilendo. Apatu tukuona kuti, Paulo sakulankhula za chilankhulo chosamveka kapena kuti chopanda tanthauzo.

(Mawu a mavesi 14 mpaka 17, onani “Chilankhulo cha Pemphero” pa Tsamba 9).

(22) Chotero malilime akhala ngati chizindikilo, si kwa iwo akukhulupira, koma kwa iwo osakhulupira; koma kunenera sikuli kwa iwo osakhulupira, koma kwa iwo amene akhulupira.

(23) Chifukwa chache, ngati Mpingo wonse akasonkhane pamodzi, ndi onse akalankhule malilime, ndipo akalowemo anthu osaphunzira kapena osakhulupira, kodi sadzanena kuti mwayaluka? (24) Koma ngati onse anenera, ndipo alowamo wina wosakhulupirira kapena wosaphunzira, atsutsidwa ndi onse; aweruzidwa ndi onse.

Cholinga chenicheni cha mphatso yakulankhula chilankhulo chachilendo chinali kuti chikhale chizindikiro kwa osakhulupirira kuti amve uthenga ndi kulandira chipulumutso monga zinalili patsiku la Pentekosti. Ngati anthu aliyense akuyankhula zilankhulo zosiyanasiyana, kaya mwaphatso kapena mochiphunzira, anthu osadziwa (amene sakumva chilankhulocho) kapena osakhulupirira afika, adzayesa kuti mwapenga chifukwa cha chisokonezo. Ndi bwino kulalikirira m'chilankhulo cha anthu osakhulupirira kuti amve ndi kupulumutsidwa.

Mu mavesi 26 mpaka 28, Paulo akupitiriza kuyankhula za chisokonezo chimene sichimalemekeza ndipo adapereka malangizo. Ngati mukulankhula chilankhulo chachilendo, muone kuti pali anthu amene amamva chilankhulocho. Ngati palibe omasulira, osalankhula m'tchalitchi mungolankhula ndi Mulungu.

Kudziwa kuti kulankhula “malilime” koona kunali kulankhula ndi

munthu wosakhulupirira m'chilankhulo chake popeza kulemekeza kwake kumafotokozera momveka za chisokonezo chimene abwera nacho anthu ku mau amene ali pa 1 Akorinto 14. Mau akuti “*Glossa*” kalelo amatanthauza komanso lero atanthauza chilankhulo chachilendo osati zolankhula zosamveka. Paulo adatsiriza pakunena ku mpingo kuti kuyankhula chilankhulo chachilendo sikunali koletsedwa, koma kuti pakhale munthu womasulira. “Koma zonse zichitike koyenera ndi kolongosoka” (1 Akorinto 14:40).

-mws



**Ngati ndalankhula m'malilime
Ndi mu chilankhulo chosadziwika,
kodi zimenezi zimatanthauza kuti
sindinapulumsidwe?
Nanga ndichite chiyani?**

Sikutembereredwa kukhala ndi kuwala kwa choonadi kuunikira m'miyoyo yathu. Koma, pamene tivomereza choonadi, timapeza mtendere ndi chigonjetso chachikulu mwa Mzimu Woyera. Monga chiphunzitso chilichonse chonyenga, pakhoza kukhala osadziwa amene alibe chidziwitso cha Mau a Mulungu. Mdani ndiwochenjera ndipo adakola ambiri ndi mchitidwe wake wa chinyengo.

Mudzifufuze moyo wanu pamaso pa Ambuye. Kodi mukukhala moyo wopanda uchimo kapena mukuchitabe ntchito za thupi? Ngati m'moyo mwanu muli uchimo, mukuyenera kulapa. Ngati mukuchita za kuyankhula zosadziwika (*glossolalia*) kapena muli ndi chilankhulo chanu chapadera mukamapemphera, muyenera nthawi yomweyo kufunafuna Mulungu kuti mumasulidwe. Izi sizitanthauza kuti zimenezi zawerengedwa kwa inu ngati uchimo ngati simudziwa za choonadi ichi, koma kuti chidziwitso cha choonadi chimatithandiza kuti tikhale odalilika. Tsoka kwa iwo amene amasiya kuunika nkumatsatira machitidwe a chikunja.

Mupemphe Mulungu kuti akukhululukireni ndi kukupatsani mtendere wa m'maganizo kapena mzimu umene wakupangitsani kuti muzichita zimenezi. Mulungu adzakukhululukirani ndi kukumasulani kuchokera ku mzimu wina uliwonse wachilendo. Muli mphamvu mu pemphero logwirizana ndipo kungakhale kopindulitsa kuti wina apemphere nanu kuti mumasulidwe ku mzimu wachinyengo wa malilime.

Chingakhale chinthu cha nzeru kuti musiyiretu kupembedza ndi ena amene amaphunzitsa ndi kuchita zimenezi ndi kudzichotsa ku chikoka/mphamvu yake. Funani chiyanjano chatsopano ndi anthu ena a umulungu amene akukhala mwachiyero ndi mchoonadi.

Mulungu akupatseni nzeru, kumasulidwa kwa uzimu mwa mwazi wa Yesu ndi mphamvu ya Mzimu Woyera. Amen.

-mws



KODI MUKUDZIWA?

Mchitidwe olankhula malilime ndi kuwatanthauzira ukuchokera kunthawi ya kale ndithu tsiku la Pentekoste lisanafike ndipo magwero ake si a chikristu. Kubwebweta mobwerezabwereza kumachitika pakati pa zipembedzo zachikunja za kale komanso za lero ndipo kukufanana ndi kulankhula zinthu zosadziwika zimene zikuchitika m'matchalichi ambiri a chi Pente masiku ano.

Izi zimachitika mu zipembedzo komanso maiko ambiri padziko lino. Zimapezeka pakati pa Akatolika, ansembe a chipembedzo cha chi Buddha, a chipembedzo cha chi Shaman ku Ethiopia ndi ku Haiti. Izi zimachitikanso pakati pa anthu a ku Japan amene amalosera zakutsogolo ndi pakati pa zipembedzo zamakolo kuno ku Afrika ndi zina zambiri.



Mau a pa
Nyengo Yake

Kankhirani

KUTI MUTIPEZE

The Gospel Truth
605 Bishops Ct.
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.us

"Kankhira kwa kuya, nimuponye makoka anu kukasodza." Luka 5:4

Ophunzira a Khristu anali atagwira ntchito molimbika usiku wonse kuyesetsa kuti agwireko nsomba. Anthu awa amene anali asodzi odziwa bwino ntchito yawo sizinawayendere ndipo panalibe chilichonse chimene anakola ngakhale ndi chule yemwe. Yesu anawauza kuti "KANKHIRANI...nimuponye makoka anu kukasodza."

Nthawi zambiri timawedza, kapena kugwira ntchito ya Ambuye, malo omwewo pamodzi ndi anzathu. Akhoza kukhala malo amene ifeyo tikuwamva kukoma koma mdalitso wake ukhoza kukhala wochepa ndipo timangowedza zochepa zedi kapena mwina osawedzako nkomwe. Ndizotheka kungokhala pamodzimodzi koma nkumavutikabe ndi ntchito ngati mmene adachitira ophunzira.



Pamene Yesu watipatsa mau, sitienera kuopa koma kupita mwa chikhulupiriro. Tiyenera kupita ku malo atsopano kumene anthu ali ndi njala ya uthenga wabwino. Yamikani Mulungu pamene munakhala chete. Atumikireni ena pamene muli mkati mwa kulingalira. Mwina kusintha kwake kwa zinthu kukhoza kukhala kochepa chabe, ndipo nthawi zina kukhoza kukhala kwakukulu, komabe mu zonse, mumvere Ambuye.

Pali nsomba zina zimene sitidzatha kuzigwira komanso pali ntchito ina imene sitidzakwanitsa kuyigwira. Tikhoza kuyankhula ndi kupemphera mmene tingathere komabe nsomba sizidzagwirika mpaka titapita ndi kukaponya makoka athu. Tisamuyikire malire Mulungu koma tiyende molingana ndi chifuniro chake. Tikasiya zonse m'manja mwa Mulungu, zotsatira zake zimakhala madalitso ochulukira, mphamvu, kud zodza, ulemerero ndi miyoyo yatsopano.

Kankhirani kwakuya mzangawe ndi kuponya makoka kuti muwedze.

-mws